# LIU LA NAMIKANGO

## Namikango Mission

**Volume 20(2), December 2020**

Ndizovuta kumvetsa kuti chaka chija chafikanso kumapeto. Chaka chimenechi chakhala chapaderadera poona zomwe zaoneka mkatikatimu. Matenda a Coronavirus asintha kachitidwe ka zinthu pa dziko lonse. Ife ngati otumikira m'dziko lina, tinalephera kubwelera ku Malawi chifukwa maulendo onse a pa ndege anaimitsidwa kotero tinakakamizidwa kukhalabe ku America. Tikayang'ana m'mbuyomu miyezi ngati yomweyi chinali chinthu cha chilendo ndi chodabwitsa kuona munthu atavala chophimba kumaso. Koma pano kuvala chophimba kumanso chasanduka chikhalidwe pena pali ponse. Ngakhalenso chizolowezi chopatsana moni wa dzanja chasintha pofuna kupewa kufala kwa matendawa.

Mukayang'ana mu chaka chimenechi muona kuti moyo wanu wasintha pakachitidwe kazinthu mwina chifukwa cha coronavirus kapena zina. Ngati mutalingalira momwe zinthu zinaliriri mu mwezi wa December 2019, nkutheka kuti mukhonza kulephera kukhulupilira zomwe zaoneka mu chaka chino cha 2020. Dziko lonse la pansi lasintha modabwitsa kwambiri ndipo likupitilira kusintha. Kusinthaku kwa khuza anthu okhala madera onse kuphatikiza kumudzi ndipo aliyense akukumana ndizosatira za kusinthaku, popeza njira zomwe angapitilire kukhalira, ngakhale pali kusintha.

Kumayambiliro kwa chaka chilichonse maka maka mwezi wa January, nthambi yoona za maphunziro ku Namikango Mission, imakhala pansi ndikubwera ndi mutu omwe umaphunzitsidwa mu chaka chonse. Chaka chino mutu wa maphunziro unali "Kupenyetsetsa pa Yesu Khrsitu" kuchokera mu buku la a Heberi. Kunena zoona unali mutu wabwino kwambiri polingalira zomwe zaoneka mu chakachi. Sitinadziwe kuti tidutsa muzimenezi koma mutu wa maphunzirowu unagwirizana ndi nyengo zomwe timadutsamo chifukwa anthu amalimbikitsidwa kuyang'ana kwa Yesu Khristu mu nthawi yovutayi. Tinganene kuti dziko lapansi lakomana ndi zinthu zambiri. Zina mwa zinthu zikulu zikulu zomwe zaoneka ndi kufala kwa matenda a coronavirus ndi zisankho za pulezidenti, matenda ena, maliro ndi zina zambiri zomwe takumana nazo. Koma mwa zonse chomwe sichinasinthe ndi chikondi cha Mulungu Atate pa ife.

Yesu anaphunzitsa kuti, Mulungu Atate amasamala ana ake ndikuwamvetsera. Atate amene amapereka zosowa za ana ake ndi kuwachiza ku nthenda zao. Atate yemwe amafunafuna ana ake ndikuwabweretsa ku nyumba. Yesu anafotokoza kuti cholinga chake ndikufuna kuonetsera chomwe Mulungu ali monga Atate wa tonse. Posatengera kuopsa kapena kukula kwa zomwe tingakumane nazo m'moyo ngakhale muliri wavuta dziko lonsewu. Choti tidziwe, Mulungu Atate ndiye nthathwe lathu komanso kochokera mphamvu zathu. Ndikukhulupilira kuti muchakachi mwapenyetsetsa kwa Yesu osati mavuto omwe takumana nawo. Chifukwa mwa Mulungu Atate mupezamo chiyembekedzo, mtendere, mphamvu ndi chimwemwe.

-Eric Gephart

# Kuyang'anitsitsa pa Yesu

Okondedwa mutu umene takhala tikugawana chaka chino ndi Kuyang'ana pa Yesu. Pa nthawi ino tafuna kuti tigwiritse ntchito mau amene tawerenga mu Chichewa cha lero amene akunena za kuyang'anitsitsa pa Yesu. Ndibwino kuyang'ana pa Yesu komanso ndi bwino koposa pamene tiyang'anitsitsa pa Yesu.

Kuyang'anitsitsa kukutanthauza kuti munthu ali kuyang'ana pa chinthu kapena munthu mwa chidwi osaganizira china chiri chonse, koma chokhacho chimene akuchiyang'anacho ndipo maso ndi maganizo samachokapo pa chimene ukuchiyang'ana. Kumakhala kuyang'ana kochikhumbira komanso kuchikonda chinthucho. Ngati chitakhala chirombo kapena china choopsya, kuyang'anitsitsa kumakhala ku mbali yoziteteza iwe mwini. Umayang'anitsitsa kuti uone kuti kodi chaima bwanji? Kodi chikundiona? Chikachoka pamenepa chilowera kuti? Kodi pali malo oti ndikhoza kuthawirako kapena kupulumukirako; ndi mafunso ena ambiri amene munthu umadzifunsa wekha cha mu mtima.

Mu phunziro lathu tikhala tikuyankha mafunso monga Chifukwa chiyani tiyenera kuyang'ana pa Yesu, ndi ndani amene ayenera kuyang'anitsitsa pa Yesu? Nanga ubwino wakuyang'ana kapena kuyang'anitsitsa pa Yesu ndi wotani? Mu bukhu la Machitidwe a Atumwi 3:3 – 6. Pamene iye (munthu wolumala) anaona Petulo ndi Yohane ali pafupi kulowa anawapempha iwo ndalama. Iwo anamuyang'anitsitsa iye. Kenaka Petulo anati, "Tiyang'ane ife!" Munthuyo anawayang'anitsitsa kuyembekezera kuti alandira kanthu kuchokera kwa iwo. Petulo anati kwa iye, "Ine ndilibe siliva kapena golide, koma chimene ndiri nacho ndikupatsa. Mdzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti, yenda!"

Chinthu china chimene tikuchiona pa kuyang'anitsitsa ndi choti pamakhala chiyembekezo chabwino. Pamene Petulo anamuuza munthu wolumala uja kuti tiyang'ane ife, iye anawayang'ana ndi chiyembekezo kuti alandira ndalama. Kodi inu abale pamene muyang'ana kwa Yesu mumayembekezera

> ### Aheberi 12:1-2
>
> Popeza kuti ponse pozungulira pali mboni zambirimbiri chotere, tiyeni tichotse kalikonse kotichedwetsa, makamaka tchimo limene limatikangamira, ndipo tithamange ndi Khama mpikisano umene tayambawu. Maso athu azipenyetsetsa Yesu amene ali woyambitsa chikhulupiliro chathu, ndiponso wochifikitsa pake penipeni. Chifukwa cha chimwemwe chimene chinkamudikira, Iyeyo adapilira zowawa zapamtanda. Adawanyoza manyazi a imfa yotere, ndipo tsopano akukhala ku dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu.

chiyani? Mzathu wolumala uja anayembekezera kulandira ndalama koma pamene anayang'anitsitsa pa Petulo ndi Yohane analandira chinthu chachikulu choposa ndalama, ndicho machiritso ake. Ife tonse tiri nako kusowa ndipo tikusoweka kuti Yesu atithandize. Mwina sitimafika pamaso pa Yesu ndi chosowa chathu chachikulu koma zazing'ono basi. Pamene Petulo anamuuza kuti tiyang'ane ife anali kufuna kuti mau onena za Yesu wa ku Nazareti kuti amuchiritsa amveke bwino ndipo autse chikhulupiriro mwa munthu wodwala uja. Akanayang'ana kumbali kapena kwina zikanakhala ngati uthenga wa Petulo ndi Yohane sukumukhudza ndipo sukanakhala wake. Kupezeka kwa Petulo ndi Yohane pamalopa kunali kupezeka kwa Yesu mwini kuti amuchiritse munthu wodwalayu kuti onse awone kuti wachiritsidwa mu dzina la Yesu.

Mu chipangano chakale mu Numeri 21: 6 – 9 tikuonanso nkhani ina yothandizira phunziro lathu lino. "Pamenepo Yehova anatumiza njoka za moto (za ululu woopsya) pakati pa anthu, ndipo zinaluma anthu; nafapo anthu ambiri a Israeli. Ndipo anthu anadza kwa Mose, nati, Tachimwa, popeza tinanena motsutsana ndi Yehova ndi inu; pempherani kwa Yehova kuti atichotsere njokazi. Ndipo Mose anawapempherera anthu. Pamenepo Yehova anati kwa Mose, upange njoka ya moto, nuiike pa mtengo wache; ndipo kudzali kuti onse

olumidwa, akaipenya njokayo adzakhala ndi moyo. Ndipo Mose anapanga njoka ya mkuwa, naiika pa mtengo; ndipo kunali, njoka itamluma munthu aliyense, nakapenyetsetsa iye pa njoka ya mkuwa, nakhala ndi moyo". Ambiri amene analumidwa ndi kuyang'ana pa njoka ya mkuwa anachiritsidwa. Panalinso ena ambiri amene atalumidwa sanayang'ane pa njoka ya mkuwa, ananyozera ndipo anafa pomwepo.

Mu bukhu lathu la Nyimbo za Mulungu tiri nayo nyimbo nambala 81 imene imanena kuti ukapenya kwa Yesu uliko moyo uko. Davide mu Masalimo 27: 4 ndi 5 akunena motere, "Chinthu chimodzi ndinachipempha kwa Yehova ndidzachilondola ichi: Kuti ndikhalitse m'nyumba ya Yehova masiku onse a moyo wanga, Kupenya kukongola kwake kwa Yehova ndi kufunsitsa m'kachisi wake. Chifukwa kuti pa dzuwa la tsoka Iye adzandibisa mu msasa mwake: Adzandibisa m'senjezi mwa chihema chake; Pa thanthwe adzandikweza".

Pakuganizira zomwe Davide akunena pa mavesi awiriwa poyamba tikuona kuti iye akupempha kuti akhale pafupi ndi Mulungu azingoyang'ana kapena kuyang'anitsitsa kukongola ndi ubwino wa Mulungu. Ichinso ndi chinthu chochititsa chidwi kwambiri. Mwina tikanakhala ife tikanapempha kuti Mulungu atithandize pa vuto lathu lina lake kaya mavuto a za chuma kapena matenda. Kwa Davide anali ndi mwayi woti akanatha kupempha kuti Mulungu agonjetse adani ake onse ndi kuti ufumu wake ukhale wodziwika pa dziko lonse. Taonani okondedwa, Davide akuti angofuna kuti aziwona kukongola kwa Mulungu. Sakupempha china chili chonse ayi.

Chinthu chachiwiri chimene akutionetsera ndi chakuti pamakhala tsiku la tsoka ndipo likadzafika, ndi Yehova amene ati adzamubise mu hema mwake. Onse amene amayang'ana pa Yesu amakhala ndi kothawira kapena pobisalapo pamene zinthu sizikuyenda bwino. Kodi inu okondedwa abale mumayang'ana kwa ndani kuti mupeze mayankho a zosowa zanu?

Aheberi 13: 5, 6. "Mtima wanu ukhale wosakonda chuma; zimene muli nazo zikukwanireni; pakuti Iye anati, Sindidzakusiya konse, kungakhale kukutaya, sindidzakutaya ndithu. Kotero kuti tinena molimbika mtima, Mthandizi wanga ndiye Ambuye; sindidzaopa; Adzandichitira chiyani munthu"? Chuma ndi chabwino koma munthu amene akuyang'ana pa Yesu chuma sichikhala chopambana kuposa Yesu. Amakhutira ndi zimene Mulungu wapereka m'moyo wake ndipo ngakhale zochepa zimakhala zokwanira. Mulungu amakhala thandizo nthawi zonse. Samadera nkhawa kapena kuchita mantha chifukwa amadziwa kuti Mulungu ali kusamalira pa zosowa ndi zovuta zonse. Nkhawa amakatula kwa Yesu – 1 Petulo 5: 7. Munthu amene akuyang'ana pa Yesu amakhala wokhutira ndi kupezeka kwa Yesu m'moyo wake ndipo zina zonse zimakhala zongoonjezeredwa ndi Yesu yemweyo – Mateyu 6: 33.

Zimamvetsa chisoni kuti anthu ambiri amapembeza ndipo amafuna kupulumuka komatu sayang'ana kwa Yesu ponena za chipulumutso chawo. Ubwino wa kuyang'ana kwa Yesu ndi woti pamodzi ndi moyo, ife timapezako zonse zomwe ndi zosowa pa moyo wathu ngakhale wa thupi. Nkofunika kuyang'ana pa Yesu ndi chikhulupiriro – Yohane 3: 36. "Aliyense amene aika chikhulupiriro chake mwa Mwana ali ndi moyo wosatha, koma iye amene samvera Mwana sadzauona moyo, pakuti mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye."

Chikhulupiriro chimakhala ngati chingwe kapena makwelero mwinanso ngati mlatho womwe umatilumikizitsa ndi zabwino za Mulungu. Ngati tingayang'ane kwa Yesu izi zimakhala zotheka mwa chikhulupiriro. Monga mwa malemba sitingathe kukondweretsa Mulungu popanda chikhulupiriro. Sizingatheke kuyang'ana kwa Yesu wopanda chikhulupiriro. Chimakhala ngati chiphaso chokatifikitsa pafupi ndi Mulungu ndi kutengapo moyo wosatha.

Kwa osakhulupirira kapena amene asankha kuti asayang'ane kwa Yesu malemba akuti, "wosakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, chifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. Koma chiweruziro ndi ichi, kuti kuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti ntchito zawo zinali zoipa. Pakuti yense wakuchita zoipa adana nako kuunika, ndipo sakudza kwa kuunika, kuti zingatsutsidwe ntchito

zake. Koma wochita choonadi adza ku kuunika, kuti ntchito zake zionekere kuti zinachitidwa mwa Mulungu." Yohane 3: 18 -21.

Anthu amene amakonda chilungamo ndipo amayang'ana kwa Yesu, amadana ndi tchimo ndipo safuna kuliyandikira chifukwa akuyenda mkuwala mwa chikhulupiriro chawo pa Yesu Khristu.

Amene sakonda Mulungu sangathe kuyang'ana kwa Yesu popeza palibe chimene amaonapo ndipo zimangokhala ngati nthano zotayitsa nthawi chifukwa alibe chikhulupiriro. Ambiri mwa iwo ndi amene amanena kuti kulibe Mulungu ndipo sakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Akadwala kapena kukumana ndi vuto lina liri lonse amathamangira ku zinthu zomwe iwo amazidalira monga asing'anga ndi zithumwa. Ena amadalira mizimu ya makolo awo amene anafa kale kuti ndiyo iwathandize powapatsa mwayi ndi kusintha nyengo zawo zovuta. Nthawi zonse amakhala ndi mantha pamene nyengo zawo sizikuyenda bwino. Sakhala okhazikika mu mtima mwawo. Choopsya kwambiri chimakhala choti nthawi zonse amakhala ndi kumayenda, koma mkwiyo wa Mulungu uli pa iwo. Ngakhale amaoneka abwino bwino osadwala, akhozanso kukhala ochita bwino pa bizinezi kapena moyo wao wa tsiku ndi tsiku, komabe tsiku lawo la tsoka lidzafika ndipo adzasowa kothawira.

Mwayi ulipobe kwa onse amene afuna kusintha makhalidwe awo ndi kuyamba moyo watsopano woyang'ana ndi kudalira Yesu. Sitingathe kuyang'ana kwa Yesu nkumachita zofuna zathu. Tikayang'ana kwa Yesu, ndi Iyeyo amene amakhala wolamulira wa moyo wathu. Amalamulira mayendedwe athu ndi zokhumba zathu. Nthawi zonse timachita zimene Iye akufuna kuti tichite osati zimene ife tikufuna. Tikayang'ana kwa Yesu, moyo wathu umakhala m'manja mwake ndipo ndi Iye amene amausamala ndi kuuteteza. Nkhawa zathu zonse timakazitula kwa Yesu – 1 Petulo 5: 7. Ngati zitakhala kuti zikumabwerabe timakatulabe komweko osasiya kukatula. Woyang'ana kwa Yesu sataya mtima msanga. Amadziwa kuti Ambuye wanga alipo ndipo akundiona, akudziwa zimene ndikudutsamo.

Potsilidza aliyense amene ayang'ana kwa Yesu amakhala wokondwa nthawi zonse ndipo mtendere wa Khristu umalamulira mu mtima mwake – Afilipi 4: 4 – 7 Paulo akulangiza mpingo wa Khristu wa ku Filipi kuti: "Nthawi zonse khalani wokondwa mwa Ambuye. Ndikubwerezanso; khalani wokondwa! Onetsetsani kuti kufatsa kwanu kuzindikike ndi anthu onse. Ambuye ali pafupi. Musadere nkhawa pa kanthu kalikonse koma mu zonse, mwa pemphero ndi chidandaulilo pamodzi ndi chiyamiko, perekani zopempha zanu kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu, umene upambana kudziwa konse udzateteza mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu." (Chichewa cha lero).

Munthu woyang'ana kwa Yesu amakhala wodabwitsa chifukwa chakuti pamodzi ndi kupempha zosowa, amakhalanso ndi nthawi yoyamika Mulungu ngakhale pa nthawi yomwe zinthu sizikuyenda bwino. Izi ndi zimene zimapangitsa kuti azikhala ndi mtendere, umene umateteza ndi kulamulira mu mtima mwake mwa Khristu.

Okondedwa musachotse maso anu auzimu ndi maganizo anu pa Yesu. Yang'anani pa Yesu kuti mukhale ndi moyo wosatha.

-Symon Katete

## HIV/EDZI ndi Utumiki wa Mpingo

Chiwerengero cha anthu amene akudwala matenda a HIV ku Malawi chili pa mndandanda wa maiko amene ali ndi chiwerengero chokwera kwambiri pa dziko lonse, anthu 9 pa 100 aliwonse; ichi ndi chiwerengero cha anthu akuluakulu (zaka 15 mpaka 49) ali ndi matendawa zimene zili zaka zotenga gawo kwambiri kuthupi komanso moyo wa uzimu. Mu chaka cha 2018, anthu pafupifupi 1million anali ali ndi kachilombo ka HIV ndipo a Malawi 13,000 anamwalira ndi matenda okhudzana ndi EDZI ndipo ambiri mwa iwo ankakhulupilira Mulungu ndipo anali a Khristu. Kachilombo ka HIV ku Malawi kamatenga gawo lalikulu pa zaka zimene munthu amakhala ndi moyo, zaka 61 kwa amuna ndi 67 kwa anthu akazi.

Mu zaka khumi zapitazo, pakhala pali kuyesetsa kufuna kuchepetsa mlili wa EDZI ngati dziko komanso maiko akunja. Mu 2018, anthu 90 pa 100 aliwonse ku Malawi amadziwa kuti ali ndi kachilombo ka HIV, mwa anthu amenewa 87 pa 100 aliwonse anali akulandira chithandizo cha mankhwala. Mwa anthu amenewa, 89 mwa anthu 100 mphamvu ya kachilomboka inali itachepetsedwa, kutanthauza kuti dziko linali litayandikira myezo wa bungwe la UNAIDS wa 90-90. Izi zikupangitsa kuti anthu 78 mwa 100 aliwonse amene ali ndi kachilombo ka HIV m'Malawi kukhala pa thandizo la mankhwala a (ART) ndi anthu 69 pa 100 aliwonse mwa onse amene ali ndi kachilombo ka HIV mphamvu ya kachilomboka kuchepetsedwa. Pakati pa ana kuyambira pa 0 mpaka zaka 4 zakubadwa amene amalandira chithandizo cha mankhwala chiwerengero chawo ndi chotsika 61 mwa 100 aliwonse amene ali ndi kachilomboka kukhala ndi kuthekera kopeza mankhwala a ART. Chiwerengero cha anthu otenga matenda chatsika kwambiri kuchoka pa 66, 000 mu chaka cha 2005, kufika pa 38, 000 mu 2018 chimene chilibe chiwerengero chachikulu. Njira yopewera kupatsirana matenda pakati pa mayi ndi mwana (PMTCT) m'Malawi yapangitsanso kuchepetsa chiwerengero cha ana amene akutengera matenda a HIV pakati pa ana a (0 mpaka 14 zaka zakubadwa). Mu chaka cha 2018 kunali makanda otenga matendawa koyamba okwana 3,500, pakuyerekeza ndi 15,000 mu chaka cha 2010. Mliri wa HIV ku Malawi's chiwerengero chake chimangophatikizidwa chonse, kutanthauza kuti mliriwu umakhudza anthu onse komanso magulu amene ali pachiopsezo kwambiri kutenga matendawa. Kupanga zogonana kosadziteteza pakati pa anthu okwatira komanso anthu ongokhalira limodzi zimenezi zimabweretsa chiwerengero cha matenda otengedwa kumene onse a kachirombo ka HIV (anthu 67 pa anthu 100 aliwonse mu 2015), ngakhalenso kungogonana kwa chisawawa kosadziteteza kumafikitsanso ku chiwerengero chambiri ndithu cha anthu otenga matendawa (anthu 12 pa 100 aliwonse mu chaka 2015). Palinso magulu ena monga atsikana achichepere, amayi, ndi azimayi oyendayenda (mahule) alinso pa chiopsezo kwambiri ku matenda a HIV. Izi zikuonetsera kuti mpingo uli ndi udindo waukulu pakulimbana ndi HIV pakuti ambiri amene ali ndi matendawa komanso kutenga ndi mamembala ake. Taganizani makanda okwana 3500 kutenga matenda chifukwa chakuti mpingo wakhala chete. Ndi nthawi tsopano kuti Mpingo wa Akhristu ukhale ndi udindo.

Mishoni ya Namikango kudzera ku pologalamu yake ya Maphunziro a Zaumoyo Akudera (Community Health Education program) (CHE) ikugwira ntchito molimbika kuthandiza mipingo kuti ikhale ndi chidziwitso cha HIV ndi EDZI komanso m'mene tingalimbirane nayo mwa uzimu. Tikukhulupilira kuti ndi mpingo okha umene ungathane ndi mliriwu motheratu chifukwa mpingo umaphunzitsa m'mene anthu angakhalire bwino, chikondi, kukhulupirika, ndi chilungamo. Namikango ikuitana mipingo yonse imene ili ndi chidwi ku maphunziro a HIV ndi EDZI amene amachitika m'masiku anayi. Mu chaka chino cha 2020 kufikira pano mipingo 17 yaphunzitsidwa za HIV ndi EDZI ndi maphunziro a mipingo kufikitsa chiwerengero cha oyimilira mipingo okwana 120 amene tsopano ali ndi udindo ophunzitsa mamembala anzawo za HIV ndi EDZI komanso za udindo wa mpingo ndi mamembala ake pakuthandizira pa nkhani ya HIV ndi EDZI. Maphunziro amenewa amalunjika pa, kumvetsetsa za HIV ndi EDZI, m'mene HIV ndi EDZI imakhudzira mpingo ndi kufalitsa uthenga wabwino, udindo wa mpingo pa nthendayi komanso m'mene tingakhalire ndi banja losangalala. Tsopano anthu ayamba kuyamikira kugwirizana kwa pakati pa kupewa kuyenera kwa HIV ndi kukhulupirika ku moyo wa uzimu chifukwa maphunzirowo amatsindika pa njira za kapewedwe ka HIV ndi kusamalira anthu odwala EDZI. Kafukufuku kuchokera ku mabungwe osiyanasiyana, a Khristu ndi anthu amene ali pa chiopsezo kwambiri chifukwa mpingo wakhala uli chete kwa nthawi yaitali kusiya anthu awo kupeza uthenga kuchokera kwa mabungwe omwe sali a Chikhristu zimene kumapeto kwake zimapangitsa kuti matendawa adzifalikira kwambiri ndi anthu kutenga kachiromboka. Kuonjezera apo, a Khristu akhala akusala anthu amene ali ndi kachiromboka ndi maganizo akuti onse amene ali ndi kachiromboka anakatenga kudzera ku makhalidwe

a uchimo ndi makhalidwe oyendayenda.

Chaka chino, ngakhale kuti tayesetsa kuti tifikire anthu ambiri ndi uthenga wa uzimu wa HIV ndi EDZI ndi njira zopewera, pologalamuyi ikukumana ndi chotchinga chimene chakhudza dziko lonse. Tili pakati pa nkhondo, kulimbana ndi covid 19 imene ikuoneka kuti siikutha pompano. Njira zopewera zikutsatidwa kulimbana ndi mliri wa covid 19. Sitikuyeneranso kuiwala za matenda akalekalewa amene atengera anthu ambiri ku manda. Ndizophweka komanso zosavuta kuiwala kuti m'mipingo mulinso anthu amene ali ndi kachirombo ka HIV amene akufunikira thandizo mu nyengo ya Covid19. Abale, pamene tikupempherera kulowerera kwa Ambuye pa Covid19 tikuyeneranso kukumbukira kupemphera ndi kulimbana ndi HIV ndi EDZI. Iyi si nkhondo yathu yokha ndi yanunso, mukhoza kutenga mbali pakupanga dongosolo loti pakhale maphunziro pa mpingo wanuwo ndi kuitana aphunzitsi athu kudzakuthandizani ndi zophunzitsa. Amene akufuna kudziwa zambiri zokhudza kapangidwe ka maphunziro ingoimbani pa 0882 790 391 ndipo tidzakutsogolerani. Mulungu akudalitseni.

-Faith Lewis Somanje

## Falless Kolopa Awona Ulemerero wa Mulungu Kudzera mu VSL

La chinayi pa 30 July 2020, ndinali ndi mwayi oyendera gulu losunga ndi kubwereketsana ndalama lotchedwa Chisomo, lomwe limapezeka pa Mpingo wa Khiristu Otchedwa Kadzuwa m'dera la dzaone, mfumu Yaikulu Chikowi m'boma la Zomba. Pa tsikuli gululi linali kugawana ndalama zomwe anakhala akusunga kwa miyezi isanu ndi inayi (9). Pamene ndinali kuyandikira pamalo omwe gululi limakumana, ndinamva nyimbo za chimwemwe. Awatu anali mamembala agulu kukondwera kuti tsopano nthawi yolandira ndalama zomwe akhala akusunga kwa nthawi yaitali yakwana. Mwambowu utatha ndinacheza ndi mayi Falless Kolopa yemwe ndi m'modzi wa mamembala a gulu la chisomo.

Ndikutuluka mu m'dima waumphawi umene wandizungulira kwa zaka zambiri tsopano.. Ine ndi banja langa takhala pa umphawi wadzaoneni , koma kudzera mu VSL, ndaona mdalitso wa Mulungu. Mayi falles adafotokoza nkhani yawo chimwemwe chitadzala tsaya.

Mai Falles kolopa, adakwanitsa kusunga ndalama zokwana 40,000 kwacha ndipo patsikuli adalandira ndalama zokwana 83,000 kwacha. Chidwi changa kwambiri chinali chakuti, kodi Mayi Falles Kolopa aigwilitsa ntchito bwanji 83,000 yomwe iwo aipeza? Atafunsidwa, iwo adayankha monyadira kuti 'ndigula mbuzi zitatu, matumba afeteleza komanso ndalama yotsala igwira ntchito zina zothandiza kuti banja langa lipite patsogolo. Cholinga chomwe ndidalowera Gulu la VSL lomwe linakhazikitsidwa ndi Namikango Mission mkuonetsetsa kuti banja langa likukhala m'moyo wa chisangalalo. Mbuzi zomwe ndikuyembekezera kugula zikachuluka, zidzandithandizira kulipira fizi ya ana anga, komanso kundithandiza m'mavuto osiyanasiyana omwe akhoza kubwera mwadzidzidzi.

Ndinali okondwa kwambiri kumva momwe mayi Fallesi Kolopa akonzekera kugwilitsa ntchito ndalama yawo. Koma funso langa linali lakuti kodi mayiwa akwanilitsadi masomphenya amenewa? Ndimaona ngati akungoyankhula zonsezi pongofuna kundisangalatsa chifukwa zimatheka munthu ukakhala ndi ndalama, umatha kuyankhula zambiri koma osakwanilitsa kanthu. Mai Falles anatsimikiza mtima za ganizo lawo ndipo anati iwo akagula mbuzi andidziwitsa nsanga. Ine ndi iwo tinagwilizana kuti tsiku la Mulungu lotsatira, pa 2 August 2020 ndikasonkhane ku Mpingo wa Kadzuwa komwe iwo amasonkhana ndicholinga choti ndidzaone mbuzi zimene anati pofika patsikuli akhala atagula.

M'mawa wa pa 02 August 2020,ndinanyamuka kupita ku dzaone monga mwa mgwilizano wathu. Mwambo wa mapemphero utatha ndinapita kunyumba kwao. Ukutu ndidawapeza iwo ndi amuna awo akundidikira. Ndikuyandikira, ndidaona mbuzi ziwiri

zitamangidwa pamtengo pafupi ndi nyumba yawo. Nditafika, iwo ndi amuna awo adafotokoza kuti panthawiyo apeza mbuzi ziwiri zokha ndipo yotsalayo anati igulidwa posachedwa. Ine ndinali okondwa kwambiri poona kuti masomphenya awo ayamba kukwanilitsidwa ndipo moyo wawo wayamba kusintha.

Chosangalatsa china m'chakuti, gulu la chisomo lidathandiza mpingo wa Kadzuwa ndi ndalama yokwana 7000 kuti ithandizire kugwira ntchito za pampingo. Abusa a Byson, Achiotcha komanso alaliki achimwanza mogwilizana adathokoza gululi kamba ka thandizoli ndipo iwo adalimbikitsa anthu ena omwe Sali mugulu kuti atha kuyamba ndikumatukula miyoyo yawo komanso kuthandiza ntchito ya Ambuye kupita pa tsogolo.

Nkhani ya Fallesi Kolopa ndi chitsanzo chimodzi chokha cha anthu ochuluka chomwe chikuonetsa momwe azimayi komanso azibambo akupindulira ndi banki ya m'mudzi Yomwe Namikango Mishoni inakhazikitsa. Anthu ochuluka ali ndi umboni kuti chiloweleni VSL, ali ndi katundu amene poyamba analibe. Akukwanitsa kusunga ndalama tsopano pagulu pomwe paokha zinali zovuta m'mbuyomo, pa gulu akukwanitsa kuthandiza osowa komanso kutukula ntchito za pamalo a Mpingo.

Poyang'ana zabwino zambiri zomwe magulu osunga ndikubwereketsana ndalama akubweretsa ku mpingo komanso midzi yosiyanasiyana kuno ku Malawi, ndikudandaulirani abale ndi alongo kuti nanuso mutha kuyambapo ntchito yosunga ndikubwereketsana ndalama mdera lomwe inu mukupezeka ndicholinga chakuti nanu mupindule ndi ntchitoyi. Yakwana nthawi tsopano kuti ife tonse tidzitulutse tokha mu nsinga za umphawi wadzaoneni umene wakuta chiwerengero chachikulu cha dziko lathu la Malawi posadalira chithandizo chochokera kwina.

Pomaliza, ndafuna kutengerapo mwayi kukumbutsani abale ndi alongo owerenga kuti kuli mliri umene wagwa maiko ambiri kuphatikizapo kuno ku Malawi otchedwa COVID 19. mliriwu wakhudza ntchito zaboma zosiyanasiyana komanso kwakukulu yakhudza ntchito ya Mpingo, monga taona kale kuti misonkhano yampingo sikuchitika, anthu tikukumana ochepa kusiyana ndi masiku apitawo pomwe nthendayi kunalibe. Ndiundido wathu ngati Mpingo kuonetsetsa kuti tikutengapo gawo potsatira ndondomeko zomwe azachipatala akutiuza kuti tithane ndi mliri umenewu. Zina mwa ndondomekozi ndi monga kusamba m'manja pafupipafupi ndi sopo, kuvala chotchinga pakamwa ndi mphuno (Masiki), kukhala motalikirana, kupewa kugwirana manja pamene tili kupatsana moni ndi zina zambiri. Ife ngati Mpingo ndiudindo wathu kuomba lipenga pamene kwagwa mliri ngati uwu.

Malemba ochokera pa 2 Mbiri 7:14 akutilimbikitsa motere; Ndipo anthu anga otchedwa dzina langa akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka mtima kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'mwamba, ndikukhululukira choipa chawo ndi kuchiritsa dziko lawo.

Masalimo 46:1 akuti, Yehova ndiye pothawirapo pathu ndi Mphamvu yathu, Thandizo lathu lopezekeratu m'masautso.

Mu malemba onsewa, ife Akhiristu taonetsedwa udindo umene tili nawo umene ukhoza kuthandizira kusintha zinthu. Davide wationetsera kumene ife tingathawire mu nthawi yosautsa monga iyi. Iye wati, mkoyenera kuti ife tithawire kwa Yehova amene ali thandizo lathu lopezekeratu mu nthawi yosautsayi. Monga Mpingo tithandizire kuthana ndi matendawa popemphera zolimba kupempherera iwo amene akudwala komanso kupempherera kuti Mulungu apitilize kuteteza iwo amene sanapezeke ndi matendawa.

COVID 19 sinthabwala, ngakhale iwo okhulupilira akudwala komanso kumwalira. Tiyeni titengepo gawo pothana ndi nthendayi.

AMBUYE AKUDALITSENI
-Styford Blazio

# Zolengeza

**Maphunziro**

- Sukulu ya Namikango ya Discipleship Training Institute (DTI) idzatsekulidwa chaka cha mawa. Tsiku lotsekulira tikuuzani posachedwapa.
- Ma fomu ofunsira malo a DTI alipo ndipo amene ali pa banja komanso amene sali pa banja ndi olimbikitsidwa kuti alembere. Aliyense amene ali ndi chidwi akhoza kulumikizana ndi Ofesi yolembetsera kudzera pa: 0885 11 43 13 kapena email:stanley@namikangomission.org

**Kufikira Anthu Ena**

- Namikango Bible School inachititsa maphunziro a atsogoleri ochokera m'magome odzungulira Blantyre. Maphunzirowa anachitikira pa 26 September, 2020 pa Mpingo wa Chirimba ndipo atsogoleri okwana 324 anachita nawo maphunzirowa.
- Mu Boma la Salima kunalinso maphunziro a atsogoleri omwe anachitikira pa Kamuzu Road Church of Christ pa 31 October, 2020. Atsogoleri okwani 203 anachita nawo maphunzirowa.

**Anthu Odwala**

- Mlogo Chidothi ochokera ku mudzi wa Mwembere, Mfumu Yaikulu (T/A) Chikowi Zomba akudwala ndipo akufunikira mapemphero.

**Omwalira**

- Mwachisoni tikukudziwitsani kuti m'bale Pichesi Jana mlaliki wachikulire kuchokera ku Namiwawa ku Zomba, anamwalira pa 10 September ndipo anaikidwa m'manda pa 11 m'mudzi wa Chinangwa Mfumu Yaikulu (T/A) Mwambo Zomba.